الحج المبرور ليس له جزاء إلا الجنة

"Ndipo Hajj Imene Iri Yabwino Iribe Dipo Lina Posakhala Jannah"

TIWONGOLERANE ZA

HAJJ

(Mu Chichewa)

Olemba:
Qullab Jim
Bukhu lakhonzedwa ndi
Ramadhan Nu'man Abu Bakr Isa
Latsindikidzidwa mu
www.malawiummah.com

Za Mkatimu

Gawo	Mutu	Tsamba
Gawo Loyamba	Hajj ndi chiyani …….....	**3**
	Kutanthauza kwa Hajj ……...	**3**
	Nyumba ya Ka'bah ……	**4**
Gawo Lachiwiri	Hajj ndi Mchitidwe wakalekale …….....	**9**
	Kukakamizidwa kwake …….....	**10**
	Kusiyana kwa Hajj ndi Umrah …….....	**14**
Gawo Lachitatu	Mitundu ya Hajj ..…….....	**15**
	Malo Osonkhanirana …….....	**15**
	Kukonzekera …….....	**17**
	Ihram …….	**17**
Gawo Lachinayi	Tawaaf (Kuzungulira Ka'bah) …….....	**20**
	Kuyenda Ndawala Pakati pa Saffa ndi Marwah	**21**
	Kuchoka ku Makkah kupita ku Minah ……..	**22**
	Kuyima pa Phiri la Arafah ……	**22**
	Kugona usiku pa Muzdalifah ……	**23**
	Nsembe …….	**23**
	Tawaaful Ifaadah (Tawaaf ya gulu) ……..	**24**
	Tawaaful Wada' …….....	**24**
	Kukayendera manda a Mtumiki salla Allah alaih wasallam ……...	**25**
Gawo Lachisanu	Ubwino ndi kufunikira kwa Hajj ……..	**26**
	Kupsyopsyona mwala wakuda ……..	**31**
	Mathero …….....	**32**

Gawo Loyamba:

Hajj ndi Chiyani?

Poyambilira ndikumuyamika Allah Subhaanah wa Ta'ala Mbuye wa zolengedwa zonse. Yemwe anayipanga Hajj kukhala imodzi mwa nsichi zomwe zamanga chipembedzo cha chisilamu yomwe mkati mwake Asilamu amaphunzira mgwirizano, chikondi komanso kukhalira limodzi wina ndi nzake. Madalitso ndi mtendere zipite kwa Mtumiki wathu Muhammad yemwe anatiwongolera ife ku njira yowongoka. Komanso madalitso ndi mtendere zipite kwa aku banja lake, ophunzira ake ndi onse omwe anamuthandiza iye kufalitsa chipembedzo cha chisilamu kufikira tsiku la chiweruzo.

Ndizachidziwikire kuti nsichi za chikukhulupiliro cha chipembedzo cha chisilamu zilipo zisanu zomwe ndi kukhulupilira mwa Allah, Angelo ake, mabuku ake, atumiki ake, komanso tsiku la chiweruzo. Kumugwadira Allah kumachitika kudzera mu zichitochito zosiyanasiyana monga kuyimika mapemphero, kupeleka chopeleka, kusala chakudya, komanso kukapanga mapemphero a Hajji ku Makkah. Chikhulupiliro ndiye tsinde la mchitidwe wina uliwonse womwe umasonyeza kumugwadira Allah komanso tsinde la zichitochito zonse mchipembedzo cha chisilamu.

Kutanthauza Kwa Hajj

Kupita ku Hajji ngati imodzi mwa nsanamila za chipembedzo cha chisilamu, ndi nchitidwe wakapembedzedwe wakale kwambiri omwe unkachitika pofuna kumugwadira ndi kumupembedza Mulungu. Hajj ndi liwu la chinenero cha chiluya lomwe limatanthauza kuchoka pamalo ndikupita kumalo ena ndi cholinga chofuna kukachita chinthu china chake. Pamalamulo a chipembedzo cha chisilamu, Hajj imatanthauza kupita ku nyumba yolemekezeka ya Ka'bah ku Makkah ndi cholinga chofuna kukachita ndi kukakwaniritsa mapemphero a Hajj.

Chifukwa choti Hajj iri ndi miyambo yambiri yomwe imawoneka ngati ndiyovutirapo kwa anthu ambiri, ndinaganiza kuti chinali chinthu chofunikira kwambiri kuwafotokozera anthu zamiyamboyi ndicholinga choti azikhala odziwa. Ndizowonadi kuti Hajj iri ndi miyambo yambiri, Koma ine pankhaniyi ndafotokoza mwachidule ndi cholinga choti wina

aliyense athe kumvetsetsa mosavuta. Choncho ngati zitapezeka kuti zinthu zina sidzinafotokozedwe, ndikupempha kuti tiyenera kubwelera ku mabukhu akuluakulu omwe anafotokoza mwatsatanetsatane zankhaniyi.

Nyumba ya Ka'bah

Tisanafotokoze za malamulo a Hajj, ndikofunikira kwambiri kwa Asilamu kudziwa angakhale mwachidule zokhudzana ndi mbiri ya nyumba ya Ka'bah yomwe malingana ndi m'mene ikutifotokozelera Qur'an yolemekezeka ndi malo omwe Asilamu amayang'anitsa nkhope zawo akamachita mapemphero awo yomwe pachinenero cha chiarab imatchedwa kuti ***Qibla*** komanso ndi malo omwe Asilamu amakachitirako miyambo yawo ya mapemphero a **Hajj**. Qur'an yolemekezeka ikutifotokozera mwatsatanetsatane motere:

"Choncho tikutembenuzira ku chibula chimene ukuchifuna: Tero titembenuzira nkhope yako yako kumbali yamsikiti woyera (Al-kaaba). (2:144)'

Mukulankhula kwinanso Allah akulankhula motere M'bukhu Lake:

"Ndithudi nyumba yoyamba yomwe idakhazikitsidwa chifukwa cha anthu kuti azipempheramo ndi yomwe ili m'maka, yodalitsidwa ndiponso ndi chiongolo kwa anthu onse. M'menemo muli zizindikiro zowonekera zozindikiritsa kupatulika kwake ndi ukale wake, ndi pamalo pomwe Ibrahim adali kuyimilira, ndipo omwe akulowamo amakhala mchitetezo. Ndithudi Mulungu walamula anthu kuti akachite Hajj mnyumbayo, amene angathe kukonza ulendo wonka kumeneko" (3:96-97) .

Mbiri ya nyumba yolemekezeka ya Ka'bah yomwe anthu amayikonzera ulendo ndi cholinga chofuna kukakwaniritsa mapemphero komanso miyambo ya Hajj, ikubwelera ku nthawi ya Mneneri Ibarahim mtendere ndi madalitso zikhale pa Iye ndi mwana wake Ismail. Mzinda wa makka omwe mkati mwake mukupezeka nyumba yolemekezeka ya Ka'bah ndi umodzi mwa mizinda yakalekale yodziwika kwambiri padziko lapansi, kuyambira kale mpakana lero. Mahadith' a Mtumiki madalitso ndi mtendere zikhale pa iye amanena mwatchutchutchu kuti tsinde komanso

gwero la nyumba imeneyi ndi Mneneri Ibarahim komanso mwana wake Ismail mtendere ukhale pa iwo.

Malingana ndi Hadith' ya Mtumiki salla Allah alaih wasallam, zikufotokozeredwa kuti Mneneri Ibrahim anamuyika mwana wake wamamuna Ismail pamodzi ndi mayi wake Hajar, pachigwa chomwe lerolino pakupezekapo mzinda wolemekezeka wa Makkah. Panthawyi nkuti dera limeneli linali kwalokha komanso lopanda zinthu zoliyenereza kuti anthu akhoza kulitenga ngati malo okhala. Iye anawasiyila iwo zina mwazipatso za tende ndi madzi pang'ono, kenako anamupempha Allah kuti akhale mtetezi komanso muyang'aniri wa iwo ndikutinso awapatse iwo zowanenereza pa moyo mdera lopanda chonde ngati limeneli.

Zimanenedwa kuti chifukwa chomwe chinamupangitsa iye kuti amutenge mwana wake Ismail pamodzi ndi mkazi wake Hajar ndi kukamuyika kudera limeneri, kunali kufuna kupewa mikangano yapabanja. Izi zinali choncho chifukwa choti mkazi wake wamkulu ***Sarah***, anayamba kuwonetsa zizindikiro za nsanje pambuyo pa kubadwa kwa ***Ismail*** yemwe anali mwana wake oyamba kuchokera kwamkazi wake wachiwiri ***Hajar***. Izi zinali chonchi chifukwa choti Sarah anakhala nthawi yayitali asanakhale ndi mwana, koma pamapeto pake muchifundo komanso chisomo cha Mulungu, iye anamubalira Ibrahim mwana wake wachiwiri yemwe ndi Ishaqa.

Ismail pamodzi ndi mayi wake anakhala modalira zipatso zatende komanso madzi omwe Ibrahim alaih salaam anawasiyira kwa masiku angapo, koma pamene madzi anawathera, Hajar anayamba kufunafuna madzi m'malo ozungulira derali. Iye anali kuchita izi pokwera komanso kutsika mapiri awiri odziwika bwino omwe ndi ***Safaa*** komanso ***Marwah.*** Iye atalephera kuwapeza madzi anabwelera komwe kunali mwana wake Ismail. Atabwelera, iye anali odabwa kwambiri powona kuti pansi pa mapazi a Ismail panayamba kutuluka kasupe wamadzi. Madzi amenewa amatuluka kuchokera ku kasupe amaneyu yemwe pamapeto pake anasandulika chitsime chosaphwa chomwe chimadziwika ndi dzina loti ***Zamzam.***

Kenaka gulu la mtundu wa anthu otchedwa ***Jurhum*** lochokera cha kum'mwera lomwe linali paulendo opita ku Syria, linawapeza anthu awiriwa komanso madzi omwe anali nawo. Ndipo gulu limeneri

litawona madzi omwe anapezeka pamalo pomwe panali Ismail ndi mayi ake Hajar, anaganiza zoti azikhalira limodzi ndi iwo. Malingana ndi m'mene Hadith' ikufotokozera, izi zinali zotsatira za mapemphero omwe Ibrahim alaih salaam anawapemphera iwo kwa Mulungu.

Kenaka Ismail anakula mumtundu wa anthu a Jurhum ndipo anaphunzira chilankhulo chawo cha Chiarab komanso zikhalidwe ndi miyambo yawo, pamapeto pake iye anakwatira mwa iwo.

Nthawi zambiri, Ibarahim anali kupita kukamuyendera Ismail pamodzi ndi mayi ake Hajar. Mu ulendo wake wina okawayendera iwo, Ibrahim analota maloto omwe mkati mwake anali kulamulidwa kuti ayenera kumupeleka nsembe mwana wake Ismail. Pomwe maloto amenewa anali kupitilira, Ibrahim anatsimikiza kuti malotowa linali lamulo lowona lochokera kwa Allah. Kenaka iye anamutenga mwana wake Ismail yemwe panthawiyi anali mwana wamng'ono kupita naye kumalo apaokha. Iye anamufotokozera mwanawake kuti Iye anali kulamulidwa ndi Allah kuti amupeleke iye nsembe pofuna kumva maganizo ake. Ismail pokhala mwana waulemu komanso omvera, sanawiringule m'malo mwake anadzipereka pofuna kukwaniritsa lamulo la Allah pa iye. Ngakhale kuti Ibrahim anali ndi chikondi chonse pa mwana wake Ismail, anatsimikiza zomuzinga mwana wake ndicholinga chofuna kumupeleka nsembe. Kenaka kunabwera lamulo lochokera kwa Allah lomulamula iye kuti apeleke nsembe nkhosa kukhala ngati chiwombolo cha mwana wake. Qur'an yafotokoza za nkhani imeneyi mu Sura 37 kuyambira pa ndime 99 kukafika 113 motere:

"Ndipo Ibrahim adati: Ndithu ine ndikupita kwa mbuye wanga, Iye andiwongolera. O Ambuye wanga! Ndipatseni mwana yemwe adzakhale m'modzi wa olungama. Ndipo tidamuwuza nkhani yabwino ya mwana wofatsa (Ismail). Ndipo (Adabadwa ndi kuyamba kukaula) pamene adakwana nsinkhu woyenda pamodzi ndi tate wake (pochitachita zamdziko Ibrahim adayesedwa mayeso kudzera m'maloto omwe iye adalota). Adati mwana wanga! Ine kutulo ndikuwona maloto owona ochokera kwa Mulungu omwe akundilamula kuti ndikuzinge monga nsembe yopeleka kwa Mulungu. Nanga ukuti bwanji? (Mwana wabwino adanena) Bambo wanga! Kwaniritsani chimene mukulamuridwa. Ngati Mulungu afuna, mundipeza ndiri m'modzi mwa opilira". Pamene adagonjera onse

awiri chofuna cha Mulungu, ndipo Ibrahim adamgoneka chakumphumi (ndipo adatsimikiza kumupha). Ndipo Tidamuyitana: E: Iwe Ibrahim! Ndithu wavomereza maloto (choncho usamuphe mwana wakoyo). Umo ndi momwe timawalipilira ochita zabwino. Ndithu amenewa ndi mayeso oonekera. Ndipo Tidampulumutsa pompatsa nyama yayikulu (yoti apeleke nsembe). Ndipo Tidansiyira nkhani yabwino kwa anthu ena (omwe adadza pambuyo pake). Mtendere ukhale pa Ibrahim. M'menemo ndi momwe timawalipilira ochita zabwino. Ndithu Iye adali m'modzi mwa akapolo athu okhulupilira. Ndiponso tidamuwuza nkhani yabwin yoti akhala ndi mwana otchedwa Isihaqa; Mneneri wa mgulu la olungama. Ndipo tidamdalitsa iye ndi mwana wake Isihaqa.* ***(37:99-113).

Nsembe imeneyi ndi chitsanzo chabwino cha chikhulupiliro chokhwima kwa anthu. Izi zikuwonetsa kuti Allah samamupondereza wina aliyense mwa anthu, koma kuti nthawi zina amawapatsa iwo mayesero ndi cholinga chofuna kuwayesa pa chikhulupiliro chawo. Ndipo amene amakhala ndi chikhulupiliro chenicheni mwa Mulungu, amakhala ndi chida cholandilira chifundo, chisoni, mtendere, chisangalalo komanso chiwongoko cha Allah.

Maulendo obwerezabwereza omwe Hajar, mayi wa Ismail anayenda pakati pa mapiri a Saffa ndi Marwah pomwe iye ankafunafuna madzi a mwana wake, komanso nsembe ya Ismail yomwe inawomboledwa ndi nkhosa, zinasanduka imodzi mwa miyambo ya mapemphero a Hajj yomwe anthu ochita Hajj amapanga.

Ibrahim anali osangalala kwambiri powona kuti mwana wake Ismail anakhazikika ku Makkah. Tsiku lina iye anamuwuza mwana wake kuti iye walamulidwa kuti amange nyumba komwe anthu okhulupilira adzikapangira mapemphero awo pofuna kudziyandikitsa ndi chisangalalo cha Allah. Ismail anawathandiza bambo ake kumanga nyumba ya ngodya zinayi, yomwe imadziwika lero lino ndi dzina loti ***Ka'bah.*** Qur'an yolemekezeka ikufotokoza zankhaniyi motere:

"Ndipo kumbukiranso pomwe Ibrahim ndi Ismail ankakhazikitsa maziko a nyumba (uku akupempha kwa Mulungu): O Mbuye wathu! Tilandireni ntchito yathuyi. Ndithudi inu ndinu wakumva Wodziwa". (2:127)

Kenaka Ibrahim alaih salaam anamupempha Allah kuti awupange mzinda wa Makkah kukhala otetezedwa komaso opambana, ndikutinso anthu ochokera madera onse adziko lapansi adzakhale akupita ku Makkah kukachita mapemphero awo odziyeretsa wokha kwa Allah pa nyumba ya Ka'bah. Qur'an yolemekezeka ikufotokoza motere:

"Ndipo kumbukani pamene Ibrahim adanena: "Mbuye wanga! Uchiteni mzinda uwu wa Makkah kukhala wa mtendere, ndipo ndipatuleni ine ndi ana anga kumchitidwe opembedza mafano. Mbuye wanga! Ndithu mafano awa asokeretsa anthu ambiri, choncho amene wanditsata, ndithudi iyeyo ali mwa ine (mudzamulipira chabwino monga mwandilonjeza), Ndipo amene wandinyoza (Mutha kumukhululukira), Ndithu inu ngokhululuka kwambiri, Ngwachisoni. Mbuye wanga! ndithu Ine ndaikhazika ina mwa nyumba yanga (mwana wanga Ismail) pachigwa ichi cha Makkah chopanda zomera panyumba yanu yopatulika (Al-Ka'bah), Mbuye wathu aloleni kuti akhale opemphera swala, choncho ichiteni mitima ya anthu kukhala yopendekera kwa iwo (akonde kudzakhala malo amenewo), ndipo apatseni zipatso kuti athokoze. (14:35-37).

Gawo Lachiwiri

Hajj Ndi Mchitidwe Wakalekale

Qur'an yolemekezeka ikutifotokozera kuti Mneneri Ibrahim adalamulidwa ndi Allah kuti alengeze ndi kuwawuza anthu za Hajj, omwe mu lamulo la Mulungu adzavomera kuyitana kwa Mwini lamulo ndipo adzakonza maulendo kuchokera madera osiyanasiyana kupita ku Makkah pogwiritsa ntchito njira za kayendedwe zosiyanasiyana. Ndipo kumeneko azikapanga miyambo ya Hajj, kupemphera mapemphero, kudyetsa osauka, ndi kupeleka chopeleka. Qur'an yolemekezeka ikufotokoza motere:

***"Ndipo kumbukirani pomwe tidamnkhazikitsa Ibrahim ndi kumulondolera pamalo pa nyumba yopatulikayo tidamuwuza kuti:" Usandiphatikize ndi chilichonse: Ndipo Iyeretse nyumba yanga chifukwa cha amene akuyizungulira ndikumakhala pompo (pochita mapemphero awo), ndi omwe amawerama pogwetsa nkhope zawo pansi. Ndipo (Tidamuwuza): Lengeza kwa anthu za Hajj! Akudzera ena oyenda ndi mapazi, ndipo ena ali pamwamba pa pachiweto chowonda chifukwa cha masautso a paulendo; adza kuchokera kunjira zamtalimtali. Kuti adzawone zabwino zawo, ndikuti aculukitse kutchula dzina la Mulungu m'masiku odziwika (ubwino wake), kupyolera mzimene wawapatsa monga ziweto za miyendo inayi. Ndipo idyani ina mwa nyamayo ndi kumdyetsa wovutika, osauka. Kenako adziyeretse kuzitakataka zawo, ndipo akwaniritse malonjezo awo ndikuzungulira nyumba yakale."* (22:26-29).**

Chipembedzo cha Allah chomwe chinabvumbulutsidwa kudzera mwa Ibrahim chinafalikira nthawi imeneyo mumzinda wa Makkah ndi madera onse ozungulira. Anthu omwe anatsatira chipembedzo cholungamachi anali kugwadira Mulungu m'modzi yekha ndipo sanamuphatikize iye ndi china chilichonse. Iwo anali kupanga ndi kukwaniritsa malamulo onse a Hajj motsogoleredwa ndi chibvumbulutso chomwe chinabvumbulutsidwa kwa Mneneri Ibrahim mtendere ukhale pa iye. Koma chifukwa cha kudutsa nthawi yayitali komanso chifukwa cha kusintha kwa mibado ndi miyambo, malamulo a chipembedzo chomwe chinabvumbulutsidwa kwa Ibrahim anasakanikirana ndi miyambo yachabechabe ya anthu opembedza

mafano. Ndipo izi zinapitilirabe kufikira panthawi yomwe Mtumiki wathu Muhammad madalitso ndi mtendere zikhale kwa iye anabadwa, fuko lirilonse la ma Arab linali ndi mafano omwe anali kusemedwa kuchokera ku matabwa, miyala ndi zinthu zina. Ndipo zokudzana ndi kumugwadira Mulungu, Mwini chilamulo komanso mphamvu zonse inali mfundo yopanda pake ndipo anthu sanalabade za kufunika kwa kumugwadira Mulungu m'modzi.

Machitidwe a mwambo wa Hajj anali kupitilira ngakhale kuti unali utasinthidwa posakanikirana ndi miyambo ya anthu ogwadira mafano. Izi zinali choncho chifukwa cha kufunika kwa miyamboyi makamaka pa malonda. Nyumba ya Ka'bah inasandulika chimake chopembedzerapo mafano ndipo inazunguliridwa ndi mafano osiyanasiyana malingana ndi mitundu ya Ma Arab. Ma Arab anali kuchoka madera osiyanasiyana chaka chilichonse ndi cholinga chofuna kukapanga miyambo ya Hajj komanso kukapeleka nsembe zosiyanasiyana ku mafano awo omwe anali ponseponse mnyumba ya Ka'bah. Pambuyo pa kubwera kwa chipembedzo cha chisilamu, miyambo ndi malamulo a Hajj omwe amachitika lero lino anakhazikitsidwa mchaka cha chisanu ndi chiwiri (7) pambuyo pa msamuko wa Mtumiki (sa) kuchoka ku Makkah kupita ku Madina. Panthawi imene mzinda wa Makkah unatsegulidwa mwatsopano ndi kukhala mchilamulo cha chipembedzo cha chisilamu mchaka chachiwiri, Mtumiki wathu Muhammad salla Allah alaih wasallam anayima mnyumba ya Ka'bah ndipo anayiyeretsa nyumba ya Ka'bah ku mafano omwe anali mkati mwake. Iye anayamba ndi kuphwanya mafano omwe anali mnyumbayi uku akulankhula mokweza mawu awa: ***"Chowonadi chadza ndi bodza lapita ndi kuthetsedwa".*** Kenaka iye analamula kuti mafano onse aphwanyidwe ndi kuswedwa. Umu ndi m'mene nyumba yolemekezeka ya Ka'bah inayeretsedwera kuchoka ku mafano ndikukhalanso nyumba yomupembedzeramo Mulungu m'modzi yekha kudzera m'mapemphero komanso popanga miyambo ya Hajj.

Kukakamizidwa Kwake

Hajj ndi mchitidwe wa miyambo ya kapembedzedwe ka pagulu omwe umachitika chaka chilichonse, omwe Asilamu amene ali ndi zowayenereza ndipo akhoza kukwanitsa kupanga ulendo opita ku ulendo omwe anthu amaukonza kuchokera mbali zonse za dziko lapansi kupita

ku Makkah amapita, gwero komanso tsinde la chipembedzo chomwe chinabvumbulutsidwa kwa Mneneri wathu Muhammad mtendere ndi madalitso zikhale pa Iye.

Umenewu ndi mchitidwe owonekera poyera wa kupembedza omwe umasonyeza mgwirizano ndi kusasiyana kwa Asilamu kuchokera kumbali zonse za dziko lapansi ndi cholinga chimodzi chomwe ndi kupangira limodzi miyambo ndi zichitochito zomwe zimachitika ndi cholinga chofuna kupeza chisoni, chifundo komanso mtendere ndi chisangalalo cha Allah Mbuye wa zolengedwa zonse.

Ku Makkah anthu onse omwe amakapanga Hajj, amayima mofanana, olemera kapena osauka, Atsogoleri ndi olamuliridwa, Ophunzira ndi osaphunzira, akuda ndi oyera. Kumeneko onse amavala zovala zoyera ndipo onse amakhala mozungulirana zomwe zimasonyeza kugwirizana komanso umodzi omwe iwo ali nawo mwa Allah Mwini wa zolengedwa zonse.

Kumeneko zolinga zawo zimakhala zofanana ndipo zotsatira zake zimawalimbikitsa ndi kuwapatsa iwo mphamvu zogwilira ntchito limodzi pofuna kukwaniritsa ubwino mokomera munthu wina aliyense.

Hajj ndi yokakamizidwa kwa Msilamu wina aliyense otha nsinkhu yemwe ali ndi zomuyenereza ndipo akhoza kukwanitsa kupanga ulendo opita ku Makkah mu thanzi ndi chuma.

Hajj siyokakamizidwa kwa anthu ena osakhala Asilamu, Ana komanso amisala omwe nzeru zawo sizikugwira ntchito malingana ndi momwe ananenera Mtumiki wathu Muhammad mtendere ndi madalitso zikhale pa Iye yemwe ananena kuti:

Cholembera (Chomwe chimalemba zochita za anthu padikira chigamulo chochokera kwa mwini lamulo) sichigwira ntchito kwa anthu atatu: Munthu amene akugona kufikira atadzuka, mwana mpakana atatha msinkhu, komanso wamisala mpaka atachila ku misala yakeyo".

Kukhala ndi zokuyenereza pa chuma komwe kumampanga munthu kuti Hajj ikhale yokakamizidwa kwa iye, kumatanthauza kukhala ndi zokuyenereza zotha kupanga ulendo opita ku Makkah kukapanga

miyambo ya Hajj komanso kukhala ndi chithandizo chokwanira cholisiyira banja, azibale komanso onse omwe umawayang'anira ndikuwathandiza. Lamulo limeneli silikuwakhudza anthu omwe ndi mzika za mzinda wa Makkah chifukwa choti kumeneko ndi kwawo ndiponso chifukwa choti nyumba ya Ka'bah ali nayo pafupi ndipo zokonzekera zawo zimakhala zochepa.

Ngati munthu atapanga Hajj ali mwana zimenezi sizingamuteteze iye kuti asadzakhale okakamizidwa kupanga Hajj atakula. Ngati ana atapitila limodzi ndi makolo awo ku Hajj ndipo sangakwanitse kupanga miyambo ya Hajj pa iwo okha, makolo kapena ayang'aniri awo akhoza kuwapangira miyambo imeneyi.

Munthu amene angamwalire asanapange Hajj amakhululukidwa ngati azibale ake atamupangira iye mudzina lake. Mtumiki salla Allah alaih wasallam ananena kuti: ***"Fulumirani kupanga Hajj yanu chifukwa palibe mwa inu amene akudziwa zimene zingamuchitikire mtsogolo ".*** Komanso munthu amene wakalamba kwambiri kapena ali ndi matenda osachiritsika, akhoza kupeza munthu oti akamupangire Hajj. Koma tiyenera kudziwa kuti kumupangira munthu wina Hajj sikoloredwa kwamunthu amene akumupangira nzake pokhapokha ngati munthuyo anadzikwaniritsira kale yekha lamulori.

Kukakamizidwa kwa Hajj kunanenedwa ndi Qur'an yolemekezeka motere:

"Ndithudi Mulungu walamula anthu kuti akachite Hajj mnyumbayo, amene angathe kukonza ulendo wonka kumeneko" (3:96-97) .

Komanso malingana ndi Hadith' ya Mtumiki salla Allah alaih wasallam, Abdullah Ibn Umar radhia Allah anhu ananena kuti anamumva Mtumiki salla Allah alaih wasallam akunena kuti:

"Chisilamu chamangidwa ndi nsanamila zisanu: Kuchitira umboni kuti palibe wina oyenera kupembedzedwa mwachowonadi koma Allah ndikuti Muhammad ndi kapolo ndi mtumiki wake, Kuyimika mapemphero, Kupeleka chopeleka, Kukachita Hajj ndi kusala m'mwezi wa Ramadhan". Inarandiridwa ndi Bukhar ndi Muslim".

Komanso Nasaai analandira Hadith' yomwe ikunena ku Mtumiki salla Allah alaih wasallam ananena kuti: ***"Hajj ndi Umrah (Hajj yaying'ono) ndi Jihad (Kumenyera mu njira ya Allah) kwa okalamba, ofowoka ndi akazi".***

Komanso Abu Hurairah analandira Hadith' yomwe Mtumiki salla Allah alaih wasallam ananena kuti: ***"Yemwe angapange Hajj popanda kuwononga popanga choyipa chilichonse, adzabwelera kwawo pambuyo pa kumaliza kwake Hajj opanda tchimo lililonse ngati mwana obadwa kumene". Inalandiridwa ndi Bukhar ndi Muslim".***

Hajj ndi yokakamizidwa kamodzi pamoyo wamunthu, koma kwa amene angapange powonjezera pamenepa amapanga choncho chifukwa cha kudzipeleka komanso kufuna kwake.

Nkhani inachokera kwa Abdulla Ibn Abbas kuti Mtumiki salla Allah alaih wasallam ananena tsiku lina mu kulankhula kwake Iye ananena kuti: "O inu anthu! Hajj ndi yokakamizidwa kwa inu choncho chitani (Hajj), m'modzi mwa Asilamu yemwe dzina lake ndi Al-Aqrah Ibn habis anafunsa: Mtumiki wa Allah! Chaka chilichonse? Mtumiki anati: "Ngati nditatero, ndiye kuti ikhala chikakamizo chomwe chili pansi pa mphamvu zanu. Hajj iyenera kuchitika kamodzi pamoyo ndipo amene angapange koposera kamodzi adzakhala kuti akupanga izi mwakufuna kwake".

Malingana ndi Hadith' iri pamwambayi, Hajj ndi yokakamizidwa kamodzi pamoyo wamunthu. Izi zidzakhala zowathandiza kwambiri anthu omwe ntchito zawo ndi zofunikira kwambiri ndipo palibe amene angayime m'malo mwawo pogwira ntchito zimenezo. Choncho izi zikusonyeza kuti Hajj iyenera kuchitika kamodzi pamoyo kwa anthu omwe zintchito zawo zimayima ngati iwo palibe.

Koma kwa anthu omwe zintchito zawo sizofunikira kwambiri ndipo anthu ena akhoza kukwanitsa kuyendetsa ntchito zimenezo ngati iwo atapita ku Hajj, palibe vuto lililonse kwa iwo kupanga Hajj m'mene angafunire ngati ali oti akhoza kukwanitsa kulipira maulendo onsewa komanso kuwasiyira mabanja awo zonse zofunika pamoyo wawo panthawi yonse ya kusapezeka kwawo chifukwa cha maulendo awo okapanga Hajj.

Kwa onse amene angakwanitse kupanga Hajj koposera kamodzi, ayenera kumvetsera ndi kupezerapo mwayi ndi uthenga omwe uli mu Hadith' ili pansiyi: ***"Yemwe amapanga Hajj kamodzi, amakwaniritsa zofuna zake, ndipo amane amapanga kachiwiri Amamufunitsitsa Mbuye wake, ndipo amene amapanga Hajj yake kachitatu, thupi lake ndilotetezedwa ku moto".***

Kusiyana kwa Hajj ndi Umrah

Pamene Hajj iri yokakamizidwa komanso imachitika m'miyezi yodziwika yomwe ndi Shawwal komanso DhulHijjah, Umrah (Hajj yaying'ono) imachitidwa mukufuna kwa munthu ndipo ilibe nthawi yake yeniyeni pachaka ngati m'mene iriri Hajj. Komanso Umrah siyimalira kuyima pa Arafah. Izi zikutanthauza kuti Umrah siyimatenga malamulo a Ihram pofuna kupanga Hajj usanafike mwezi wa Ramadhan. Koma Ihram ya Umrah imatha kuchitika nthawi ina iliyonse makamaka m'mwezi wa Ramadhan.

Gawo Lachitatu

Mitundu ya Hajj

Munthu ofuna kupanga hajj ayenera kutsimikiza imodzi mwa mitundu ya Hajj iri m'munsiyi asanalowe mu Ihram pofuna kupanga Hajj. Mitundu yake ndi iyi:

1. ***Ifrad*** (Yapayokha) yomwe imatanthauza kupanga Hajj yokha.

2. ***Qiran*** (Kuphatikiza) Yomwe imatanthauza kupanga Hajj mophatikiza ndi Umrah. Ndipo munthu openga mtundu wa Hajj umenewu amatchedwa kuti Qarin (ophatikiza).

3. ***Tamattu-u*** (Chisangalalo), yomwe imatanthauza kupanga kaye Umrah poyamba. Kenako munthuyo akhoza kusiya Ihram yake ndi kulowa mu umoyo wake wa nthawi zonse kufikira tsiku la chisanu ndi chitatu (8) la mwezi wa dhul Hijjah lomwe adzapitilize kupanga malamulo a Hajj . Ndipo munthu opanga mtundu wa Hajj umenewu amatchedwa kuti Mutta (Osangalala).

Imeneyi ndi mitundu ya Hajj malingana ndi Hadith' yomwe inalandiridwa ndi Mayi Aishah radhia Allah anha yomwe iye akufotokoza motere:

"Tinapangira limodzi ndi Mtumiki salla Allah alaih wasallam Hajj yake ya malawirano. Ena mwa ife tinatsimikiza za kupanga Ihram pofuna kupanga Umrah poyamba, ndipo ena anaphatikiza Hajj ndi Umrah, ndipo ena anatsimikiza za Ihram pofuna kupanga Hajj yokha".

Malo Osonkhanirana

Malo omwe anthu omwe amakapanga Hajj amasonkhana asanavale zovala zawo za Ihram pofuna kupanga Hajj kapena Umrah, ndi malo osiyanasiyana omwe ali kunja kwa mzinda wa Makka omwe anasankhidwa malingana ndi malamulo a chipembedzo cha chisilamu ndi cholinga chimenechi. Ngati anthu afika malo amenewo, iwo amakonzeka muthupi ndi uzimu pofuna kupanga ntchito yotamandika komanso yopatulika ya Hajj. Mtumiki salla Allah alaih wasallam anakhazikitsa malo amenewo kum'mwela, kum'mawa komanso kumpoto

kwa mzinda wa Makkah. Tatiyeni tiwone tsatanetsatane wa malo amenewa motere:

a. Dhul-Hulaifah: amanewa ndi malo omwe anakhazikitsidwa cha kumpoto kwa mzinda wa Makka pamtunda wa Makilomita 450. Amenewa ndi malo omwe anakhazikitsidwa kwa anthu omwe ndi mzika za mumzinda wa Madina ndi onse omwe ali cha kumpoto kwa mzindawu.

b. Rabigh: amenewa ndi malo omwe anakhazikitsidwa kwa anthu ochokera cha kumpoto kwa dziko la Syria, Lebanon, Turkey, ndi madera ena. Komanso onse ochokera kumpoto chakumadzulo monga anthu ochokera ku mayiko a ku Africa kapena omwe amadutsa ku Africa ngati akuchokera cha kumpoto cha kumadzulo.

c. Yalamlam: Limeneli ndi phiri lomwe liri cha kum'mwera kwa mzinda wa Makka lomwe Mtumiki salla Allah alaih wasallam anakhazikitsa ngati malo ofikirapo anthu a ku Yemen ndi onse ochokera kumayiko ali cha kum'mwera.

d. Qarnul-Manazil: Limeneli ndi phiri lomwe liri cha kum'mawa kwa mzinda wa Makka ndipo ndi malo omwe anakhazikitsidwa kwa anthu a mtundu wa Najd ndi onse ochokera kum'mawa.

Anthu omwe amachokera m'madera osiyanasiyana omwe ali pakati pa malo amanewa ndi mzinda wa Makkah ayenera kupangiratu Ihram yawo kumalo komwe iwo akonzekera ulendo wawo okachita Hajj.

Kwa anthu omwe ndi mzika za mzinda wa makka, ayenera kupangira Ihram yawo mnyumba zawo. Koma ngati iwo apanga Ihram ya Umrah, iwo ayenera kupita kumalo oyera ndikupanga Ihram yawo kumeneko kenako ayenera kupitiliza kupanga miyambo yonse ya Umrah.

Wina aliyense yemwe wafika pamalo ake omwe anayikidwa ngati malo ake ofikira malingana ndi dera lomwe akuchokera ayenera kukonzekera Ihram yake pamalo amenewo.

Koma chifukwa choti anthu okapanga Hajj omwe amayenda chowuluka pa ndege, sangapange Ihram yawo mundege ngati akuwadutsa madera amenewo, m'malo mwake ayenera kupanga Ihram yawo pamalo okwelera ngati akupita ku Makkah.

Kukonzekera

Ngati munthu akufuna kupanga hajj ayenera kupanga zinthu zingapo asanayambe ulendo wake. Ndipo zinthu zimenezi ziri motere:

1. Ayenera kupempha chikhululuko kwa Allah pamachimo ake onse omwe anatsogoza ndi zoipa zonse zomwe iye anatsogoza m'mbuyo. Komanso ayenera kulonjeza kuti sadzabwereza kuchita machimo amenewo mtsogolo.

2. Kuyanjana komanso kulazanitsa mitima ndi anthu onse omwe iwe unawalakwira kapena kuwapondereza munjira ina iliyonse ndi kuwapempha anthu amenewa kuti akhale okhululuka.

3. Kubweza ngongole zonse zomwe unali nazo.

4. Kulisiyira banja lako ndi onse omwe umawayang'anira ndalama kapena chithandizo chilichonse chokwana zowathandiza iwo panthawi ya kusapezeka kwako mpakana utabwelera ku ulendo wako.

5. Kudziyeretsa wekha ku makhalidwe onse oyipa ndikudziyeretsa pochita makhalidwe onse otamandika komanso abwino.

6. Uyenera kuwonetsetsa kuti wabayitsa katemera wa chikuku, kolera, ndi matenda ena komanso kulandira chitupa cha zaumoyo ku unduna wa za umoyo chosonyeza kuti thupi lako ndilangwiro komanso lathanzi.

Ihram

Usanakonzekere zonse zokhudzana ndi Ihram, lamulo la chisilamu likukupempha kuti uyenera kutsata zinthu izi:

a. Kumeta tsitsi lonse loyenera kumetedwa komanso kuwenga zikhadabo.

b. Uyenera kusamba ngati kuli kotheka komanso uyenera kudziyeretsa popanga Udhu.

c. Amuna popanga Ihram yawo ayenera kuchotsa zovala zawo zonse ndi kuvala chovala cha Ihram, chovala choyera chosasokedwa chomwe

chimavalidwa mopingitsidwa pathupi posiya nkono komanso phewa lakumanja pamtunda. Chovala cha Ihram chimakhala ndi nsalu ziwiri zosasokedwa komanso zosakongoletsedwa ndi mitundu ya mtundu wina uliwonse. Ina imamangidwa mchiwuno ndipo ina imavalidwa modutsitsa pakhosi ndi mapewa posiya phewa komanso nkono wakumanzere pamtunda. Nsalu zimenezi zili ndi mayina. Ina imatchedwa Rida ndipo ina imatchedwa Izar. Kumutu sikumavalidwa chilichonse angakhale kuti okalamba amaloredwa kumanga china chake m'mutu koma ayenera kupeleka chopeleka chomwe chimapelekedwa kwa osauka. Mapazi ayenera kukhala pantunda mpakana m'misomali, pachifukwachi nkhwayila ndi zomwe zimavalidwa m'malo mwa nsapato. Nsapato zikhoza kuvalidwa ngati sizikubisa misomali.

d. Ndipo akazi amavala chovala chovala chachitali chomwe chimayambira kumutu mpakana ku miyendo kupatula kubisa nkhope ndi zikhatho. Ndipo ndizofunikira kwambiri kwa iwo kuvala nkhwayila zomwe zimakonzedwa mwapadera kwa anthu opanga Hajj.

e. Tiyenera kuti, ngati tayenda pandege, tipange Ihram yathu tisananyamuke pamalo onyamukira.

f. Anthu onse ayenera kupemphera Maraka'at awiri ndi chitsimikizo chofuna kupanga Ihram.

Iwo akamalowa mu mwambo wa Ihram, amachita chitsimikizo chawo pantchito yodalitsikayi ponena mokweza mawu awa:

"Labbaiykallahumma Labbayka. Labbayka La Sharika laka Labbayka, Innal-hamda wanni'mata laka wal mulk la sharika laka. Omwe amatanthauza kuti:

"Ndavomera Mbuye wanga ndavomera! Ndavomera Mbuye wanga ndavomera! Mulibe opaphatikizana nanu. Ndavomera! Kutamandika ndi mtendere zonse ndi za Inu. Muli ndi ufumu onse. Mulibe ophatikizana nanu"

Tiyenera kudziwa kuti munthu amene akupanga Hajj, ngati ali mu mwambo wake wa Ihram, sayenera kukhalira limodzi ndi mkazi, kumeta tsitsi, kuwenga zikhadabo kapena kuvala chovala kumutu. Ndipo akazi adzabisa thupi lawo lonse kupatula nkhope ndi zikhatho.

Chovala china chilichonse sichimaloledwa kupatula chovala cha Ihram. Mkanjo, *Amama* , chisoti, china chilichonse chosokedwa komanso china chilichonse chokongoletsedwa ndi mitundu yosiyanasiyana sichololedwa. Ngakhale kuti akazi amaloledwa kuvala zovala za kufuna kwawo, samaloledwa kuvala zophimba zikhatho, Chophimba kumaso, komanso sayenera kugwiritsa ntchito mafuta onunkhiritsa (Perfume). Komanso sayenera kuvala zovala zowonekera mkati komanso zokongoletsa ndi mitundu yosiyanasiyana.

Choncho tawona kuti chinthu choyambilira mu zichitochito za Hajj kapena Umrah ndi kulowa m'mwambo wa Ihram womwe umasonyeza kuti munthu watsimikiza kupanga miyambo yonse ya Hajj kapena Umrah. Ndipo Gawo lina ndi Tawaf.

Gawo Lachinayi

Tawaf (Kuzungulira Ka'bah)

Tawaf ndi liwu la chinenero cha chiarab lomwe limatanthauza kuzungulira, ndipo malingana ndi malamulo a Hajj mchisilamu, liwuli limatanthauza kuzungulira nyumba yolemekezeka ya Ka'bah.

Tawaf ili m'magulu atatu:

1. **Tawaf yapofika:** Imeneyi ndi Tawaf yomwe anthu okapanga Hajj amapanga akangofika kumene ku Makkah.

2. **Tawaf ya gulu:** Imeneyi ndi Tawaf yomwe iwo amapanga pambuyo pa kupereka nsembe popha zinyama.

3. **Tawaf ya pobwelera:** Imeneyi ndi Tawaf yomwe anthu opanga Hajj amapanga panthawi yonyamuka ku Makka pobwelera kwawo.

Iwo akamapanga Tawaf (Kuzungulira Ka'bah), amakhala akudziyeretsa wokha pokalowa nyumba ya Ka'bah ndikuzungulira kasanu ndi kawiri (7) kuyambira pa mwala wakuda poyisiya Ka'bah chakumbali ya kumanzere. Ndipo pambuyo pa kuzungulira kulikonse, mwala wakuda umapsyopsyonedwa, kapena kugwiridwa kapena pongolozera mongav ngati ukuwulawira ngati kuli kotheka.

Akazi panthawi ya matenda awo akumwezi samaloledwa kupanga Tawaf. Ndipo amene ali oyeretsedwa ku matenda amenewa, akuyenera kupanga Tawaf. Uku kumayimira kulemekeza malo a Ibrahim omwe anatchulidwa mu Qur'an yolemekezeka motere:

***"Ndipo (kumbukiraninso nkhani iye) pomwe tinayipanga nyumba (ya Ka'bah) kuti pakhale pamalo pobwelerapo anthu (poyendera anthu) ndikukhalanso malo a chitetezo. Ndikuti mupachite kukhala popemphelera swala pamalo pomwe Ibrahim adali kuyimilira pomanga nyumbayo . Ndipo tidamulamula Ibrahim ndi Ismail kuti iyeretseni nyumba yanga chifukwa cha oyizungulira (pochita Tawaf) ndi amene akuchita m'bindikiro, ndichifukwa cha amene akuwerama ndi kulambira (kuswali m'menemo).* (2:125).**

Kenako Anthu amayima moyiyang'ana Ka'bah, poyima pakati pa iyo ndi pamalo pa Ibrahim pomwe amapemphera maraka'at awiri.

Kuyenda Ndawala Pakati Pa Saffa Ndi Marwah

Chinthu chinanso chomwe chimachitika popanga Hajj kapena Umrah ndiko kuyenda ndawala pakati pa mapiri awiri a Saffaa ndi Marwah. Iye ayenera kukwera paphiri la Saffa ndikuyima moyiyang'ana Ka'bah ndipo kenako ayenera kukweza manja ake pomuthokoza ndi kumuyamika Mulungu. Kenako amayenda pachipata chaching'ono kufikira atakafika pa chigwa cha pakati pa Saffa ndi Marwah komwe amayendano mwandawala komanso mofulumira. Iye akafika paphiri la Marwa, amakwera phirilo ndikuchita chimodzimodzi monga momwe anachitira pa phiri la Safa. Ndipo kuyenda mwa ndawala pakati pa mapiri awiriwa kuyenera kumachitika kasanu ndi kawiri (7) kuyambira pa phiri la Safa kukamalizira pa phiri la Marwah.

Monga momwe tafotokozera kale kuti kuthamanga komwe kumachitika pakati pa phiri la Safa ndi Marwah chimakhala chikumbutso chomukumbulikira Hajar, mayi wake wa Ismail komanso mkazi wa Mneneri Ibrahim yemwe anali kuzungulira pamalowa pofunafuna madzi a mwana wake Ismail.

Ndizofunikira kwambiri kwa onse opanga Hajj akafika pa phiri la Safa kuwerenga mawu a Allah omwe akupezeka mu Qur'an yolemekezeka motere:

"Ndithudi Safaa ndi Marwah (mapiri awiri omwe omwe pakati pake pamachitika pemphero loyenda ndawala) ndi zizindikiro zolemekezera chipembedzo cha Mulungu. Choncho amene akukachita mapemphero kunyumbayo kapena kuchita Umrah, sikulakwa kwa iye kuzungulira pamenepo (pakati pa mapiri amenewo). Ndipo amene achite chabwino modzipeleka adzalipidwa. Ndithudi Mulungu ngothokoza, ngodziwa. (2:158)

Ndipo miyambo yonse ya Umrah imatsirizika pambuyo pa kumaliza kuyenda ndawala pakati pa Safaa ndi Marwah.

Koma kwa amene anatsimikiza zopanga Hajj yokha (Ifrad) kapena kulumikiza Hajj ndi Umrah (Qiran) ayenera kukhala muzovala zawo za Ihram mpaka atamaliza miyambo yonse ya Hajj.

Koma kwa awo amene anatsimikiza za kupanga Umrah payokha popimira ndikudzayilumikiza ndi miyambo ya Hajj (Tamatu'u) pa tsiku la chisanu ndi chitatu (8) la mwezi wa Dhul-hijjah, akhoza kusiya zovala zawo za Ihram koma ayenera kuzinga chinyama chomwe chimaperekedwa kwa osauka. Ngati sanapeze choti ndikuzinga, ayenera kusala masiku atatu ali ku Hajj komweko ndipo ayeneranso kudzasala masiku asanu ndi awiri akadzabwelera kwawo. Ndipo mtundu wa Hajj wa Tamattu'u ndi opambana kwambiri poyerekeza ndi Ifrad komanso Qiran chifukwa choti mtundu wa Hajj umenewu ndi osavuta komanso Mtumiki salla Allah alaih wasallam anawuyamikira.

Kuchoka Ku Makkah Kupita Ku Minah

Patsiku lachisanu ndi chitatu (8) la mwezi wa Dhul-Hijjah, onse opanga Hajj ayenera kuchoka ku Makka ndi kupita ku Mina. Apa ndi pomwe munthu amene anatsimikiza za Hajj ya Tamatu'u amavalanso zovala zake za Ihram ndi kuzilumikiza ndi onse opanga Hajj. Masana onse ayenera kupezeka pa Mina, malo omwe ali pa mtunda wa Makilomita asanu ndi anayi kuchokera ku Makka. Kumeneko iwo amapemphera mapemphero awo a Dhuhr, Asr, Maghrib komanso Isha ndipo pamapeto pake amagona tsiku limelo pamalo amenewa.

Kuyima Paphiri La Arafah

Patsiku la chisanu ndi chinayi la mwezi wa Dhul-Hijjah, Asilamu opanga Hajj amapemphera pemphero lawo lam'mawa (Fajr) pa Mina, kenako amadikilira kutuluka kwa dzuwa. Kenako iwo amanyamuka kupita ku phiri la Arafah akulankhula mokweza mawu onena kuti ***Allah Akbar*** omwe amatanthauza kuti Mulungu ndi wamkulu. Kumeneko, iwo amapemphera pemphero la Dhuhr molumikiza ndi pemphero la Asr panthawi ya pemphero la Dhuhr.

Kuyima pa phiri la Arafah ndi umodzi mwa miyambo yotamandika komanso yofunikira kwambiri yomwe imachitika nthawi ya Hajj. Munthu osiya kupanga mwambo umenewu sanganene kuti wapanga Hajj. Ngati anthu ena utawadutsa mwambowu chifukwa cha zovuta zina

mwina chifukwa cha kuchulukana kwa anthu, ayenera kupanga madzulo angakhale m'pakana kum'banda kucha wa tsiku lachikhumi (10) lamwezi wa Dhul-Hijja.

Pokamba za ubwino wa kuyima pa phiri la Arafah, Mtumiki salla Allah alaih wasallam ananena kuti:

"Palibe Hajj kwa munthu ngati sanayime pa phiri la Arafah".

Kugona Usiku Pa Muzdalfah

Pambuyo pa kuyima paphiri la Arafa, Asilamu onse amanyamuka tsiku lomwelo kupita ku Muzdahlfah komwe amakafikako chakumadzulo dzuwa lisanalowe. Muzdalfah ndi malo omwe amapezeka pakati pa Arafah ndi Mina. Mbendera zomwe zimasonyeza malire a malo olemekezeka, zimabzalidwa. Mapemphero a Maghrib komanso Isha amapempheredwa mophatikiza.

Iwo amakhala pa Muzdalfah m'pakana usiku kufikira nthawi ya pemphero la m'mawa wa pa 10 Dhul-Hijjah. Munthawi yonse yomwe iwo amakhala ali pa Muzdalfah, amakhala akumuyamika Mulungu, kuwerenga bukhu lolemekezeka la Qur'an pamalo a chizindikiro omwe Allah anawatchula m'bukhu lake lolemekezeka la Qur'an motere:

"Ndipo mukabwelera kuchoka ku Arafah, Tamandani Mulungu pamalo otchedwa Mash'ar Haram (Muzdalfah). Ndipo mukumbukireni monga momwe adakutsogolerani. Ndithudi kale mudali mwaosochera. (2:198)"

Pambuyo pa kupemphera pemphero lakum'bandakucha (Fajr) pa 10 Dhul-Hijjah, onse amachoka pa Muzdalfah ndi kupita ku Mina uku atatenga timiyala ting'onoting'ono tomwe amakatigwiritsira ntchito pogenda zipilala za Aqaba zomwe ziri pa Mina. Munthu amene sangathe kotero chifukwa cha matenda kapena kukalamba, ayenera kupeza munthu oti akachite mwambo umenewu m'malo mwa iye.

Nsembe

Pambuyo pa kugenda zipilala zimenezi, iwo amayamba kupeleka nsembe zawo pozinga zinyama. Mazanamazana a nkhosa, mbuzi,

komanso ngamila zimakhala zitasungidwa kale ndicholinga choti ziperekedwe nsembe. Ndipo mwala waukulu omwe uli cha kumadzulo kwa chigwa cha Mina unakhazikitsidwa ngati malo chifukwa cha mwambo umenewu.

Patsiku limeneli lomwe limakhala pa 10 mwezi wa Dhul-Hijjah, Asilamu dziko lonse lapansi amapeleka nsembe zawo popha zinyama zosiyanasiyana ndiponso amasangalalira limodzi chisangalalo cha kupeleka nsembe. Ndipo munthu amene anatsimikiza za Hajj ya Tamattu'u samapeleka nsembe pokhapokha ngati atapanga ndawala pa Safaa ndi Marwah.

Tawaful-Ifadah (Tawaf Yagulu)

Onse opanga Hajj ayenera kupanga Tawaf yapagulu komwe kuli kuzungulira limodzi pagulu pa 10 Dhul-Hijjah pambuyo pa kumeta tsitsi ndi kuwenga zikhadabo. Ndipo Tawaf imeneyi ikhoza kuchitika m'masiku atatu otsatira pambuyo pa tsiku lopeleka nsembe.

Pambuyo pa Tawaf imeneyi, iwo akhoza kusiya zovala zawo za Ihram ndikupitiliza kuyamika komanso kumuyeretsa Allah.

Tiyenera kudziwa kuti Munthu amene anatsimikiza za kupanga Hajj ya Tamattu'u, sangapange Ihlal (kumuyeretsa Allah ndi kumukuza) ngati sanayende nawo ndawala pa Safaa ndi Marwah kachiwiri. Iye ayenera kudziwa kuti ndawala yoyamba yomwe iye amayenda imakhala ya Hajj.

Pambuyo pa kumuyeretsa komanso kumukuza ndi kumutamanda Mulungu, onse ayenera kubwelera ku Mina ndi cholinga choti akamalize masiku atatu otsatira pambuyo pa tsiku lopeleka nsembe ndipo m'masiku amenewa iwo ayenera kupitiliza kugenda timiyala ting'onotig'ono kuyambira masana mpakana kulowa kwa dzuwa.

Tawaful-Wadaa

Gawo lotsiriza la mwambo wa Hajj ndi Tawaful –Wadaa (Kuzungulira kolawira). Malingana ndi Hadith' yomwe anayilandira Ibn Abbas, Mtumiki salla Allah alaih wasallam analamula kuti anthu opanga Hajj omwe sinzika za M'makka ayenera kuzungulira komwe kumasonyeza kulawirana asananyamuke ku Makkah kubwelera kwawo.

Kukayendera Manda A Mtumiki salla Allah alaih wasallam

Mwambo otsirizira kwambiri pa miyambo ya Hajj ndiko malinga ndi malamulo ndi oti onse opanga Hajj ayenera kupita ku Madina kukayendera manda a Mtumiki wathu Muhammad salla Allah alaih wasallam. Panthawi yomwe iwo akulowa munzinda wa Mumzikiti wa Mtumiki ku Madina, ayenera kutchula china chilichonse chomwe iwo akuchidziwa mu zabwino za ubwino komanso kufunikira kwa Mtumiki wathu Mhammad salla Allah alaih wasallam komanso ayenera kupempha chiwongoko kwa iye pa umoyo wake wauzimu.

Pambuyo pa kulowa mumzikiti wa Mtumiki salla Allah alaih wasallam, iwo ayenera kupemphera Maraka'at awiri kenako ndi kupita ku manda a Mtumiki komwe amakanena mawu awa:

Mtendere ukhale pa inu, Mtumiki wa Allah, Ndikuchitira umboni kuti palibe wina oyenera kupembedzedwa mwachowonadi kupatula Allah, ndikuti inu ndi kapolo komanso Mtumiki wa Allah.

Komanso ndikofunikira kwambiri kwa iwo kutembenukira chakum'mawa ndi cholinga chofuna kupeleka ulemu kwa Abubakar komanso manda a Mlowa m'malo wa Mtumiki pambyo pa Abubakar yemwe ndi Umar radhia Allah anhu.

Gawo Lachisanu

Ubwino ndi Kufunikira Kwa Hajj

Munayamba mwaziwona nkhunda mazanamazana zitatera paphiri ndi mawonekedwe ake odziwika ndi aliyense, omwe amasonyeza mtendere, chikondi komanso mgwirizano?

Kumakkah, paphiri la Arafah mukhoza kukhala osangalatsidwa komanso odabwa powona chinamtindi cha anthu okapanga Hajj ochokera ku ngodya zonse za dziko lapansi omwe chiwelengero chawo chimapyola mamilioni awiri kapena kuposa pamenepa, onse atavala zovala zoyera zofanana za Ihram zomwe zimawachita iwo kuti aziwoneka ngati nkhunda zomwe zasonkhana pamalo amodzi. Ngati mutawathira diso chapatali mukhoza kuganiza kuti ndi nkhunda zomwe zasonkhana pamalo amodzi. Ndipo ngati mutawayandikira kuti muwonetsetse mukhoza kuzindikira kuti iwo ndi anthu ochokera madera osiyanasiyana omwe afika mu mzinda wa Makkah womwe mkati mwake mukupezeka nyumba yolemekezeka ya Ka'bah ndi cholinga chofuna kukavomera kuyitana kwa Ibrahim alaih salaam, lamulo la Mbuye wawo pofuna kukwaniritsa ina mwa nsanamila zomwe zamanga chipembedzo cha chisilamu. Panthawiyi iwo amawoneka ngati nkhunda mazanamazana zomwe zatera patanthwe limodzi. Iwo amakhala atanyamula manja awo uku akumupempha ndi kumuyamika Mbuye wawo pamitendere yonse yomwe iye amawonetsera zolengedwa zake komanso uku akumupempha Iye kuti ayike mtendere, chikondi komanso mgwirizano pakati pawo.

Kumeneko, paphiri la Arafah pamakhala palibe opambana kuposa mzake munjira ina iliyonse. Izi zimakhala choncho posayang'ana kupambana kwa dziko lomwe iye akuchokera, zovala zomwe iye amavala angakhalenso pachilankhulo chomwe iye amalankhula. Siungathe kusiyanitsa pakati pa M'malawi ndi Msudani, Mtchayina ndi Mmwenye, mzungu ndi wakuda, olemera ndi osauka, ophunzira ndi osaphunzira, olamula ndi olamuliridwa; m'malo mwake onse amakhala akapolo onyozeka pamanso pa Allah Mbuye wa Zolengedwa zonse.

Ndizowonadi kuti siungasiyanitse pakati pa munthu ndi nzake. Onse amakhala pa moyo ofanana, Mayiko awo amasanduka dziko limodzi,

chovala chawo chimakhala cha mtundu umodzi, Chilankhulo chawo chimakhala chimodzi. Kumeneko dziko lawo limakhala Chisilamu, Chovala chawo chimakhala Ihram, komanso chilankhulo chawo chimakhala Chiarab.

Onse amakhala akulankhula chilankhulo chimodzi povomera kuyitana kwa Mbuye wawo mokweza mawu uku akunena mawu awa:

Labbayka –Allahumma labbayka!

Ndavomera! Mbuye wanga ndavomera!

Wina aliyense amaganiza kuti ali pamaso pa Allah. Wina aliyense amaganiza kuti akamanena mawu amenewa akumulankhula Allah uku ali chiyimire pamalo pomwe panayima Mtumiki salla Allah alaih wasallam uku akupempha ngati m'mene Iye anapemphera komanso akupempha kwa Mbuye wawo ngati momwe iye adapemphera.

Anthu onse opanga Hajj panthawiyi, Wakuda ndi Oyera, Olemera ndi osauka amuna ndi akazi onse amakhala chimodzimodzi pamaso pa Allah.

Palibe chikayiko kuti chovala cha Ihram chomwe iwo amavala, ndi chovala cha chidziwitso cha mgwirizano. Iwo samavala chovala cha mtundu wina uliwonse kupatula Ihram, popanda chowonjezera chilichonse m'matupi mwawo ngati m'mene zimakhalira patsiku la kubadwa komanso patsiku lakufa.

Titangobadwa kumene, tidavekedwa chovala chimodzi, komanso tikadzamwalira tidzavekedwa chovala chimodzi. Tinabadwa amaliseche, ndipo chimodzimodzinso tidzamwalira tili amaliseche.

Choncho chovala cha Ihram ndi cha umaliseche wathu omwe umafunikira panthawi yomwe tili pamaso pa Allah. Uku ndiko kusiyana kwa kuwonekera kwa munthu pamanso pa Allah ndi pamanso pa mtsogoleri wa dziko.

Panthawi yomwe tikufuna kukawonana ndi mtsogoleri wa dziko, timawonetsetsa kuti tikhale a ukhondo komanso timayesetsa kuti tivale zovala zapamwamba. Koma panthawi yomwe tikuwonekera pamaso pa Allah, ife sikanthu, ndipo ichi ndichifukwa chake zovala zapamwamba

zili zosafunikira panthawi yokumana ndi Allah yemwe ndi Mbuye wa zolengedwa zonse.

Ichi ndi chifukwa chomwe Allah anamulamulira Mneneri wake Musa alaih salaam kuti avule nsapato zake panthawi yomwe iye anayandikira patanthwe loyera komwe iye amayembekezera kuti akumane ndi Mulengi komanso Mwini chilamulo. Nkhani imeneyi ikupezeka m'bukhu lolemekezeka la Qur'an motere:

"Ndipo kodi yakufika nkhani ya Musa (Yomwe ndi yododometsa)?. Adawuza banja lake yembekezani (pano); ndawona moto, mwina ndingakakutengereni chikuni chamoto (kuti muothe), kapena ndikapeza ondiongolera njira pamotopo. Koma pamene adaudzera motowo, Adayitanidwa (kuti) E! Iwe Musa!. Ndithu ine ndine Mbuye wako. Vula nsapato zako; ndithudi iwe uli pachigwa chopatulika, chotchedwa Tuwa. Ndipo ine ndakusankha kuti ukhale Mtumiki. Choncho mvera zonse zomwe zikubvumbulutsidwa kwa iwe. Ndithu Ine ndine Mulungu palibe wopembedzedwa mwachowonadi koma Ine, choncho ndipembeze, pemphera swala mondikumbukira. Ndithu nthawi ya tsiku lachiweruzo idza; (choncho ikonzekere ndi ntchito zabwino); ndikuyibisa dala kwa anthu kuti mzimu uliwonse udzalipidwe zimene udachita. (20:9-15)

Paphiri la Arafah, pamasonkhana anthu ochokera m'mayiko osiyanasiyana komanso amitundu yosiyanasiyana, amawonekedwe osiyanasiyana komanso a zilankhulo zosiyanasiyana kuyambira masana mpakana madzulo. Iwo amakhala akulankhula ndi Allah popanda mkhala-pakati aliyense, pamtetete popanda choyala kapena denga kupatula mpweya omwe iwo amawupeza kuchokera kumbali zonse.

Panthawi yomwe iwo ali paphiri la Arafah, amapatsana moni wina ndi nzake komanso amadziwitsana wina ndi nzake, kupanga ubale wina ndi nzake komanso kuphunzira kuchokera kwa wina ndi nzake. Umenewu umakhala msonkhano waukulu komanso opambana womwe amasonkhana anthu amiyambo komanso maudindo osiyanasiyana komanso womwe pamakhala kugawana nzeru pakati pa wina ndi nzake omwe gwero lake limakhala kuvomera kwa anthu pa kuyitana kwa Allah yemwe ndi Mbuye wa zolengedwa zonse. Izi zimatsimikiza ndi kuchitira umboni mawu a Allah omwe tikuwapeza m'bukhu lake lolemekezeka motere:

"E inu anthu! Tidakulengani (nonse) kuchokera kwa mamuna m'modzi (Adam) ndi mkazi m'modzi (Hawa) ndipo tidakupangani kukhal a mitundi ndi mafuko (osiyanasiyana) kuti mdziwane basi. Ndithu olemekezeka kwambiri mwa inu kwa Mulungu, ndi yemwe ali owopa. Ndithu Mulungu Ngodziwa ndipo Ngodziwa kwambiri nkhani zonse" (49:13)

Panthawi yomwe iwo asonkhana pa phiri la Arafah, mkwiyo umasandulika chikondi, kusiyana kumasandulika mgwirizano, amene amkapanga zoipa amasintha ndikuyamba kupanga zabwino, omwe amkakhulupilira zamabodza amasintha ndikuyamba kusankha zowona zokhazokha, anthu oyipa amasintha kukhala abwino komanso tsankho limasandulika chilungamo.

Kuphatikiza pa zonsezi, machimo onse am'mbuyo omwe munthu anatsogoza amakhala atakhululukidwa ndipo amakhala ndi tsogolo labwino chifukwa choti amakhala opanda tchimo lina lililonse. Malingana ndi Hadith' yomwe inalandiridwa ndi Jabir' alaih salaam, Mtumiki salla Allah alaih wasallam ananena kuti:

"Likafika tsiku la Arafah, Allah amawatsitsa angelo ake pamtambo otsiriza ndipo amawayamikira onse opanga Hajj pamanso pa Angelo motere: 'Tawonani akapolo anga amene adza kwa ine monyozeka, komanso otuwa omwe akulira kuchokera m'matanthwe onse. Ndikufuna kuti muchitire umboni kuti ndawakhululukira'. Kenako angelo amanena kuti: 'O Mbuye wathu! Wakuti ndi wauti amakayikiridwa chimodzimodzinso azimayi akuti ndi akuti'. Iye amati Allah yemwe ndi wapamwamba komanso otamandika wayankha kuti: 'Ndawakhululukira iwo'. Mtumiki wa Allah anati: 'Palibe tsiku lomwe anthu amatulutsidwa kumoto ngati la Arafah".

Muyenera kukumbukira kuti Hajar yemwe ndi mayi ake a Ismail ndi yemwe anayimilira azimayi onse pa m'bado uliwonse. Mwana wake anagwidwa ndi ludzu. Ndipo atawona kuti panalibe madzi, anaganiza zokafunafuna madziwo. Iye anati: "Mwina ndingakawapeze pa phiri la Safaa kapena paphiri la Marwah kapena patanthwe lapakati pa mapiri awiriwa. Iye anachita izi poyenda pamapiri awiriwa mobwerezabwereza koma sanawapeze madzi. Iye anayesetsa mwa iye yekha munjira ina iliyonse. Pachifukwachi iye analidi mayi odziwa udindo wake, kapena mukulankhula kwina tinganene kuti anali opambana kuposera mayi.

Chikondi cha mayi chomwe iye anali nacho ndi chomwe chinamupatsa iye mphamvu zoti ayende pamapiri awiriwa mobwerezabwereza ndicholinga chofunafuna madzi othetsera ludzu la mwana wake ndipo iye nali ndi chikhulupiliro chonse kuti zingavute maka kwina kwake kuyenera kupezeka madzi. Mneneri Ibrahim yemwe ndi Mamuna wake anawasiya iwo muchisamaliro cha Allah. Ndipo Ibrahim anali ndi chikhulupiliro chonse kuti Allah awasamalira ndi kuwayang'anira iwo ndipo sizingatheke kuti awanyalanyaze ndi kuwasiya akuvutika.

Hajar atabwelera pomwe panali mwana wake pambuyo pakutopa ndi kuvutika kamba kofunafuna madzi, anali odabwa kwambiri powona kasupe wamadzi yemwe anabuka pansi pa mapazi a mwana wake ndipo iye anati monthunthwa: ***"Ndithudi madzi akutuluka pansi pa mapazi a mwana wanga. O Allah! M'dalitseni Ismail, Inu ndipo gwero la chipambano ndi chisangalalo. Mulungu akudalitse iwe Ibrahim, ndithudi unali kunena zowona".***

Wina aliyense amene amakapanga Hajj kapena Umrah , amuna kaya akazi, anyamata kapena asungwana amakhala akumukumbukira mayi olemekezeka yemwe sanataye chikhulupiliro kuti zingavute maka, madzi ayenera kupezeka kwinakwake ngangale anayenda pakati pa mapiri a Safaa ndi Marwah kasanu ndi kawiri (7).

Kuyenda kwa ndawala komwe Hajar anakuchita ndi chitsanzo chabwino kwa ife cha mavuto omwe amapezeka pamoyo. Ngati m'mene anavutikira Hajar, ndimomwenso ayenera kuchitira aliyense tsiku lina lirilonse, ndithudi umu ndi m'mene moyo umakhalira. Panthawi yomwe ife tili pamavuto, tiyenera kuyesetsa kupeza njira yothetsera vutolo, ndipo ngati titalephera ngati momwe analephelera Hajar, tiyenera kudziwa kuti Allah amakhala tcheru nthawi zonse pofuna kumva kugogoda ndi kulira kwa akapolo ake. Ndipo chisoni ndi chifundo chake chimakhala chikutidikilira ife nthawi zonse. Tamvani m'mene Allah akulankhulira m'bukhu lake lolemekezeka la Qur'an:

"Ndipo ngati Mulungu atakukhudza ndi masautso, Palibe aliyense owachotsa kupatula Iye. Ngatinso atakufunira zabwino, palibe amene angaubweze ubwino Wake. (Iye) amadza ndi ubwinowo kwa amene wamfuna mwa akapolo ake. Ndipo Iye Ngokhululuka Ngwachisoni". (10:107)

Kuwupsyopsyona Mwala Wakuda

Ina mwa miyambo yomwe imachitika panthawi ya Hajj ndiko ***kuwupsyopsyona mwala wakuda*** panthawi yozungulira nyumba yolemekezeka ya Ka'bah. Ndikofunikira kwambiri kuti tikambepo zokhudzana ndi mwambo opsyopsyona mwala wakuda pofuna kuwongolera kusamvetsa kwa anthu ena pamwambo umenewu makamaka alembi akumayiko aku wulaya omwe ndi adani a chipembedzo cha chisilamu.

Alembi amenewa amanena kuti ulemu omwe umaperekedwa ku nyumba ya Ka'bah komanso mwala wakuda ndi miyambo ya Ma Arab omwe anali kumuphatikiza Mulungu ndi zinthu zina komanso omwe amkapembedza mafano. Mbiri pa iyo yokha ikutsutsa mowonekera mfundo imeneyi ndipo ikutifotokozera kuti Ma Arab anthawi imeneyo sanali kuyipembedza Ka'bah kapena mwala wakuda omwe anthu opanga Hajj amayenera kuwupsyopsyona ngati atapeza danga panthawi yomwe akuzungulira nyumba ya Ka'bah. Komanso tiyenera kudziwa kuti nyumba ya Ka'bah siyinali mgulu la mafano omwe Ma arab amenewa anali kuwapembedza. Mwala wakuda umenewu uli ngati chikumbutso kapena chizindikiro cha mwala wamaziko omwe iye anayika panthawi yomwe iye anali kumanga nyumba ya Ka'bah. Anthu opanga Hajj samagwadira nyumba ya Ka'bah kapena mwala wakuda koma amamugwadira Allah, Mbuye wa Ka'bah ndi mwala wakuda.

Komanso ina mwa miyambo yomwe imachitika panthawi ya Hajj ndiko kugenda miyala ing'onoing'ono pa zipilala za chikumbutso za Aqaba. Kugenda komwe kumachitikaku kumakhala kukumbukira kugendedwa kwa Satana komwe kunali kuchitika ndi Ibrahim panthawi yomwe anakafuna kumunyenga kuti alephere mayeso a Mbuye wake panthawi yomwe iye analamulidwa kuti amupereke nsembe mwana wake Ismail. Komanso kumayimira kulonjeza ndi kutsimikiza kwa munthu opanga Hajjiyo kuti sadzatsatira mapazi komanso njira zosokonekera za satana, kapena kupanga ubale ndi anthu ochita zoipa kapenanso kumvera zinthu zomwe zingamuwongolere ku njira ya satana.

Tiyenera kudziwa kuti miyambo yonse yomwe imachitika panthawi ya Hajj zimathandiza kulimbikitsa chikondi komanso mgwirizano pakati pa anthu kwina kulikonse komwe angakhale. Panthawi yomwe iwo akupanga hajj, onse amakhala ofanana ndipo pamakhala palibe

opambana kuposa nzake. Sipamakhala kusiya kwina kulikonse pakati pa osauka ndi olemera, oyera ndi wakuda, ophunzira ndi osaphunzira, mtsogoleri ndi otsogoleredwa. Kusiyana kwawo konse kumatha panthawi ndipo onse amakhala ofanana ndi onyozeka pamanso pa Mbuye wawo.

Mathero

Pomaliza kufotokoza zokhudzana ndi Hajj, ndikufuna kuwakumbutsa onse amene amakapanga Hajj kuti m'mene akudziwira kuti mankhwala ozunguza bongo komanso mchititidwe uliwonse onyansa uli oletsedwa m'malamulo a chipembedzo cha Chisilamu; yeneranso kudziwa kuti kuphwanya malamulo onse omwe anakhazikitsidwa ndi dziko la Saudi Arabia kapena bungwe lina lilionse ndikoletsedwa mchipembedio cha chisilamu.

Chifukwa choti Hajj ndiko kunyamuka kupita kwa Allah ndi Mtumiki wake, ndipo anthu onse okapanga Hajj ayenera kuwonetsetsa kuti chimenechi ndi chomwe chiyenera kukhala chitsimikizo chawo. Iwo ayenera kudziyeretsa ku machimo onse komanso ku zilakolako za dziko lapansi ndicholinga choti pamapeto pa Hajj yawo ayenera kubwelera kwawo ali opanda tchimo lina lililonse ngati ana omwe angobadwa kumene.

Malingana ndi Hadith' yomwe inalandiridwa ndi Umar Ibn el-Khattab, Mtumiki salla Allah alaih wasallam anati:

"China chilichonse chiyenera kuchitika malingana ndi chitsimikizo chake ndipo wina aliyense adzakhala ndi chomwe watsimikiza. Yemwe angasamuke kupita kwa Allah ndi Mtumiki wake, amasamukadi kupita kwa Allah ndi Mtumiki wake. Ndipo amene angasamuke pofuna kupeza zamdziko kapena chifukwa cha mkazi amene akufna kumukwatira, Nsamuko wake umakhala pazomwe wasamukira".

Chisilamu sichimaletsa kupanga zinthu zolorezedwa panthawi ya ulendo wa Hajj, ngati zinthuzo zitachitika mosapyola malire pamalamulo a chipembedzo cha Chisilamu. Chimidzomodzinso ngati zinthuzo sizikutsutsana ndi malamu a dziko kapena bungwe lomwe liri ndi udindo oyang'anira zinthuzo.

Pomaliza penipeni ndikumupempha Allah kuti atipatse ife zonse zotiyenereza kuti tidzakwaniritse ina mwa nsichi zomwe zamanga chipembedzo cha chisilamu yomwe ndi Hajj. Komanso kuti awalipire ndikuwadalitsa onse omwe anakwaniritsa kale nsichi imeneyi. Komanso ndikumupempha Iye kuti akatiyike ife mgulu la akapolo ake omwe akalandire chisoni ndi mtendere wake tsiku la chiweruzo. Komanso ndikumupempha Iye kuti apereke zabwino zake zonse kwa Mtumiki wake Muhammad salla Allah alaih wasallam yemwe anatiphunzitsa ife chipembedzo chathu komanso yemwe anatiwongolera ife njira yowongoka. Komanso kuti awadalitse akubanja lake, Omutsatira ake ndi onse omwe anamuthandiza iye pofalitsa chipembedzo cha chisilamu kufikira tsiku la chiweruzo. ***Ameen!!!***

Bukuli ndi la ulere
Choncho lisagulitsidwe
Kapena kusinthanitsa ndi china chake
posakhala malipiro a Allah Subhaanah wa Ta'ala
~~~~~~
Malawi Ummah Islamic Information Website
info@malawiummah.com
~~~~~~